
# Tadala ndi Tino Agonjetsa KOLERA


Mmudzi mwathu lero mwacha bwino. Dzuwa lawala ndipo anthu akulima m'minda mwawo. Ena akugwira ntchito zawo zatsiku ndi tsiku. M'mudzimu mudali mjigo koma pano udawonongeka. Mayi a Tadala ndi Tino akufuna madzi oti agwiritse ntchito pakhomo. Choncho atuma Tadala ndi Tino kuti akatunge madzi kumtsinje.











Mmawa mwake Tadala, Tino ndi ana ena am'mudzi mwathu alawira kupita ku sukulu.... koma Tadala adabwa ndi kufowoka kwa Tino.
Tino, ulibwino koma? Ukuwoneka wofooka
Kuyambira mamawa ndikupita kuchimbudzi pafupipafupi.


Kuchimbudziko ndapita kale koposa katatu konse..


Tadala ndi Tino apita kwa Madam Banda omwe ndi mphunzitsi wawo.
Madam,Tino akuoneka wofooka! Ameneyu mwina akudwala!!
Standard 4


M'modzi mwa aphunzitsi apita ndi Tino kuchipatala pa njinga ya moto. Ndipo operekeza akwera njinga ina.
Tadala, pita akauze makolo ako kuti Tino wadwala ndipo tikupita naye ku chipatala
Head Teacher's Office
Tino wafika kuchipatala
Mwana wanu akutsekula m'mimba kwambiri mayi, ndipo wafooka. Iyi itha kukhala nthenda ya kolera...
...Koma kuti titsimikize, timuyeza ndipo anzathu opimapima akaunika ngati mthupi mwake muli tizirombo toyambitsa kolera kapena ayi.
Chabwino adokotala
Podikilira, timpatsa **ORS** poti kutaya madzi ambiri a m'thupi ndi chiopsyezo pa moyo.
Kuchokera mu zoyezayeza Tino anampeza ndi kolera.




Bukhuli latsindikizidwa ndi Unduna wa Za Umoyo ndi thandizo lochokera ku UNICEF